# Maphunziro a m'Baibulo

Bible studies

# Paulo

1. Kusandulika mtima kwa Paulo
2. Mdindo wa ku Filipi
3. Ulendo woyamba wa Paulo
4. Uthenga Wabwino ulalikidwa ku Lustra
5. Paulo ku Efeso
6. Demetriyo autsa phokoso
7. Paulo mu Trowa
8. Amtumiza Paulo ku Roma
9. Tsoka pa nyanja
10. Paulo pa Melita
11. Paulo afika ku Roma

Ngatitu mukhalabe m'cikhulupiriro, ocirimika ndi okhazikika ndi osasunthika kulekana naco ciyembekezo ca Uthenga Wabwino umene mudaumva, wolalikidwa colengedwa conse ca pansi pa thambo; umene ine Paulo ndakhala mtumiki wace – Akolose 1.23

- Stephanos Zambia Trust –
www.kudziwazamulungu.com

## 1. Kusandulika mtima kwa Paulo

**Macitidwe a Atumwi 9.1-18**

1. Koma Saulo wosaleka kupumira pa akuphunzira a Ambuye kuopsya ndi kupha, ananka kwa mkulu wa ansembe.
2. napempha kwa iye akalata akunka nao ku Damasiko kumasunagoge, kuti akapeza ena otsata Njirayo, amuna ndi akazi akawatenge kudza nao omangidwa ku Yerusalemu.
3. Ndipo poyenda ulendo wace, kunali kuti iye anayandikira Damasiko; ndipo mwadzidzidzi kudawala momzingira kuunika kocokera kumwamba;
4. ndipo anagwa pansi, namva mau akunena naye, Saulo Saulo, Undilondalonderanji?
5. Koma anati, Ndinu yani Mbuye? Ndipo anati: Ndine Yesu amene umlondalonda;
6. komatu, uka, nulowe m'mudzi, ndipo kudzanenedwa kwa iwe cimene uyenera kucita.
7. Ndipo amunawo akumperekeza iye anaima du, atamvadi mau, koma osaona munthu.
8. Ndipo Saulu anauka; koma potseguka maso ace, sanapenya kanthu; ndipo anamgwira dzanja, namtenga nalowa naye m'Damasiko.
9. Ndipo anakhala masiku atatu wosaona, ndipo sanadya kapena kumwa.
10. Koma ku Damasiko kunali wophunzira wina dzina lace Hananiya; ndipo Ambuye anati kwa iye m'masomphenya, Hananiya. Ndipo anati, Ndiri pano, Ambuye.
11. Ndipo Ambuye anati kwa iye, Tauka, pita ku khwalala lochedwa Lolunjika, ndipo m'nyumba ya Yuda ufunse za munthu dzina lace Saulo, wa ku Tariso; pakuti taona, alikupemphera
12. ndipo anaona mwamuna dzina lace Hananiya, alikulowa, namuika manja, kuti apenyenso.
13. Ndipo Hananiya anayankha nati, Ambuye, ndamva ndi ambiri za munthu uyu, kuti anacitiradi coipa oyera mtima anu m'Yerusalemu;
14. ndi kuti pano ali nao ulamuliro wa kwa ansembe akulu wakumanga onse akuitana pa dzina lanu.
15. Koma Ambuye anati kwa iye, Pita; pakuti iye ndiye cotengera canga cosankhika, cakunyamula dzina langa pamaso pa amitundu ndi mafumu ndi ana a Israyeli;
16. pakuti Ine ndidzamuonetsa iye zinthu zambiri ayenera iye kuzimva kuwawa cifukwa ca dzina langa.
17. ndipo anacoka Hananiya, nalowa mnyumbayo; ndipo anaika manja ace pa iye, nati, Saulo, mbale, Ambuye wandituma ine, ndiye Yesu amene anakuonekerani pa njira wadzerayo, kuti upenyenso, ndi kudzazidwa ndi Mzimu Woyera.
18. Ndipo pomwepo padagwa kucoka m'maso mwace ngati mamba, ndipo anapenyanso.

19 ndipo ananyamuka nabatizidwa; ndipo analandira cakudya, naona naco mphamvu.

**Mafunso**

1. Saulo anazunza anthu otsata Njirayo. Kodi ndi Njira yotani?
2. Ndi cifukwa ciani Saulo anapempha akalata kwa mkulu wa ansembe? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
3. Ndi ciani cimene cinacitika pamene Saulo anali kupita pa njira? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
4. Ndi yani amene anakamba ndi Saulo? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
5. Kodi Saulo anayankha ciani? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
6. Ndi cifukwa ciani cinali cofunikira kuti amuna anagwira dzanja la Saulo?
7. Kodi ndi yani amene anakhala ku Damasiko. Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
8. Ndi cifukwa ciani Hananiya ananyanyala asanapite kwa Saulo? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
9. Kodi Hananiya anacita ciani atafika kumene Saulo analiko? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
10. Saulo anasandulika mtima. Kodi kusandulika mtima kutanthauza ciani?
11. Kodi ndinu wosandulika mtima?

**Sewero**

Pezani mau onse.

| | |
|---|---|
| SAULO | HANANIYA |
| AKALATA | FARISO |
| DAMASIKO | COIPA |
| KUUNIKA | MASO |
| MAU | CAKUDYA |

| | | | | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| K | A | T | A | L | A | K | A | O |
| K | U | U | N | I | K | A | U | S |
| O | K | I | S | A | M | A | D | I |
| L | S | T | M | E | P | M | B | R |
| U | H | A | N | A | N | I | Y | A |
| A | U | E | M | N | U | K | O | F |
| S | A | A | Y | D | U | K | A | C |

## 2. Mdindo wa ku Filipi

**Macitidwe 16.16-34**


16. Ndipo panali, pamene tinalinkunka kukapemphera, anakomana ndi ife namwali wina amene anali ndi
mzimu wambwebwe, amene anapindulira ambuye ace zambiri pakubwebweta pace.
17. Ameneyo anatsata Paulo ndi ife, napfuula, kuti, anthu awa ndi akapolo a Mulungu wa Kumwambamwamba, amene akulalikirani inu njira ya cipulumutso.
18. Ndipo anacita cotero masiku ambiri. Koma Paulo anabvutika mtima ndithu, naceuka, nati kwa mzimuwo, Ndikulamulira iwe m’dzina la Yesu Kristu, turuka mwa iye. Ndipo unaturuka nthawi yomweyo.
19. Koma pamene ambuye ace anaona kuti kulingalira kwa kupindula kwao kwatha, anagwira Paulo ndi Sila, nawakokera kunka nao kuwbalo kwa akuru,
20. ndipo pamene adanka nao kwa oweruza, anati, Anthu awa abvuta kwambiri mudzi wathu, ndiwo Ayuda.
21. ndipo alalikira miyambo imene siiloleka ife kuilandira, kapena kuicita, ndife Aroma.
22. Ndipo linagumukira iwo khamulo; ndipo oweruza anawang’ambira maraya ao; nalamulira kuti awakwapule.
23. Pamene anawaonetsa mikwingwirima yambiri anawaika m’ndende, nauza mdindo kuti awasunge bwino.
24. Pakumva iye kulamulira kotero anawaika m’cipinda ca m’kati, namangitsa mapazi ao m’zigologolo.
25. Koma ngati pakati pa usiku, Paulo ndi Sila analinkupemphera,
nayimbira Mulungu nyimbo, ndipo a m’ndendemo analinkuwamva.
26. ndipo mwadzidzidzi panali cibvomezi cacikuru, cotero kuti maziko a ndende anagwedezeka; pomwepo pamakomo ponse panatseguka; ndi maunyolo a onse anamasuka.
27. Pamene anautsidwa kutulo mdindoyo, anaona kuti pa makomo a ndende panatseguka, ndipo anasolola lupanga lace, nati adziphe yekha, poyesa kuti a m’ndende adathawa.
28. Koma Paulo anapfuula ndi mau akuru, nati, Usadzipweteka
wekha; tonse tiri muno.
29. Ndipo mdindo anaitanitsa nyali, natumphira m’kati, alinkunthunthumira ndi mantha, nagwa pamaso pa Paulo ndi Sila,
30. nawaturutsira iwo kunja, nati, Ambuye ndicitenji kuti ndipulumuke?
31. Ndipo iwo anati, Ukhulupirire Ambuye Yesu, ndipo udzapulumuka, iwe ndi apabanja ako.
32. Ndipo anamuuza iye mau a Ambuye, pamodzi ndi onse a pabanja pace.
33. Ndipo anawatenga ora lomwelo la usiku, natsuka mikwingwirima yao; nabatizidwa pomwepo, iye ndi a pabanja pace.
34. Ndipo anakwera nao kunka kunyumba kwace, nawakhazikira cakudya, nasangalala kwambiri, pamodzi ndi a pabanja pace, atakhulupirira Mulungu.

**Mafunso**

1. Kodi mkazi wokhala ndi mzimu wambwebwe anacita ciani? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
2. Kodi Paulo anacita ciani kulingana ndi ndime ya 18?
3. Ndi cifukwa ciani ambuye a mkazi anafuna kuwaika Paulo ndi Sila m’ndende? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
4. Kodi mdindo anacita ciani kuti Paulo ndi Sila asathawe?
5. Kulingana ndi inu, ndi cifukwa ciani Paulo ndi Sila anaimbira Mulungu nyimbo?
6. Ndi ciani cimene cinacitika usiku? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
7. Kodi mdindo anafunsa ciani Paulo ndi Sila? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
8. Nanga inu mufunanso kupulumuka ku macimo anu?
9. Kodi Paulo anamyankha ciani mdindo? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
10. Kodi mdindo anacita ciani atabatizidwa? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
11. Kodi tingaphunzire ciani m’nthano iyi?

**Sewero**

Lembani mau pa malo ao.




aroma
nyimbo
mzimu
banja
akapolo
ayuda
cipulumutso
lupanga
mdindo
cipinda
sangalala
pulumuka

## 3. Ulendo woyamba wa Paulo

**Macitidwe a Atumwi 13.1-12**

1. Ndipo kunali aneneri ndi aphunzitsi ku Antiokeya mu Mpingo wa komweko, ndiwo Barnaba, ndi Sumeoni, wonenedwa Nigeri, ndi Lukiya wa ku Kurene, Manayeni woleredwa pamodzi ndi Herode ciwangaco, ndi Saulo.
2. Ndipo pa kutumikira Ambuye iwowa, ndi kusala cakudya, Mzimu Woyera anati, Mundipatulire Ine Barnaba ndi Saulo ku nchito imene ndinawaitanirako.
3. Pamenepo, m'mene adasala cakudya ndi kupemphera ndi kuika manja pa iwo, anawatumiza amuke.
4. Pamenepo iwo, otumidwa ndi Mzimu Woyera, anatsikira ku Selukeya; ndipo pocokerapo anapita m'ngalawa ku Kupro.
5. Ndipo pokhala ku Salami, analalikira mau a Mulungu m'masunagoge a Ayuda; ndipo anali nayenso Yohane mnyamata wao.
6. Ndipo m'mene anapitirira cisumbu conse kufikira Pafo, anapezapo munthu watsenga, mneneri wonyenga, ndiye Myuda, dzina lace Baryesu;
7. ameneyo anali ndi kazembe Sergio Paulo, ndiye munthu wanzeru. Yemweyo anaitana Barnaba ndi Saulo, nafunitsa kumva mau a Mulungu.
8. Koma Elima watsengayo (pakuti dzina lace litera posandulika) anawakaniza, nayesa kupatutsa kazembe asakhulupire.
9. Koma Saulo, ndiye Paulo, wodzazidwa ndi Mzimu Woyera, anampenyetsetsa iye,
10. nati, Wodzala ndi cinyengo conse ndi cenjerero lonse, iwe, mwana wa mdierekezi, mdani wa cilungamo conse, kodi sudzaleka kuipsa njira zolunjika za Ambuye?
11. Ndipo tsopano, taona, dzanja la Ambuye liri pa iwe, ndipo udzakhala wakhungu wosapenya dzuwa nthawi, Ndipo pomwepo lidamgwera khungu ndi mdima; ndipo anamukamuka nafuna wina womgwira dzanja.
12. Pamenepo kazembe, pakuona cocitikaco anakhulupira, nadabwa naco ciphunzitso ca Ambuye.

**Mafunso**

1. Werenganinso ndime ya 2. Kodi Mulungu amaitanabe anthu kuti amtumikire?
2. Chulani dzina la mneneri wonyenga. Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
3. Kazembe Sergio Paulo anafuna kumva mau a Mulungu. Kodi Elima (kapena Baryesu) anacita ciani kulingana ndi ndime ya 8?
4. Kodi m’umoyo mwanu mulinso anthu amene afuna kuti musakhulupirire? Kodi muwayankha bwanji?
5. Ndi ciani cimene cinacitika ndi Elima (Baryesu)? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
6. Kodi tingaphunzire ciani m’nthano iyi?

**Sewero**

Lembani malembo pa malo ao kukapeza yankho (Macitidwe a Atumwi 8.21).

| 13 | 20 | 9 | 13 | 1 |
|---|---|---|---|---|
| | | | | |

| 23 | 1 | 11 | 15 |
|---|---|---|---|
| | | | |

| 19 | 21 | 12 | 9 |
|---|---|---|---|
| | | | |

| 23 | 15 | 12 | 21 | 14 | 10 | 9 | 11 | 1 |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| | | | | | | | | |

| 16 | 1 | 13 | 1 | 19 | 15 |
|---|---|---|---|---|---|
| | | | | | |

| 16 | 1 |
|---|---|
| | |

| 13 | 21 | 12 | 21 | 14 | 7 | 21 |
|---|---|---|---|---|---|---|
| | | | | | | |

| 1 | 2 | 3 | 4 | 5 | 6 | 7 | 8 | 9 | 10 | 11 | 12 | 13 |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| A | B | C | D | E | F | G | H | I | J | K | L | M |

| 14 | 15 | 16 | 17 | 18 | 19 | 20 | 21 | 22 | 23 | 24 | 25 | 26 |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| N | O | P | Q | R | S | T | U | V | W | X | Y | Z |

## 4. Uthenga Wabwino ulalikidwa ku Lustra

**Macitidwe a Atumwi 14.8-20**

8. Ndipo pa Lustra panakhala munthu wina wopanda mphamvu ya m'mapazi mwace, wopunduka cibadwire, amene sanayenda nthawi zonse.
9. Ameneyo anamva Paulo alinkulankhula; ndipo Paulo pomyang'anitsa, ndi kuona kuti anali ndi cikhulupiriro colandira naco moyo,
10. anati ndi mau akuru, Taimirira. Ndipo iyeyu anazunzuka, nayenda.
11. Pamene makamu anaona cimene anacita Paulo, anakweza mau ao, nati m'cinenero ca Lukaoniya, Milungu yatsikira kwa ife monga anthu.
12. Ndipo anamucha Barnaba, Zeu; ndi Paulo, Herme, cifukwa anali wotsogola kunena.
13. Koma wansembe wa Zeu wa kumaso kwa mudzi, anadza nazo ng'ombe ndi maluwa kuzipata, nafuna kupereka nsembe pamodzi ndi makamu.
14. Pamene anamva atumwi Paulo ndi Barnaba, anang'amba zopfunda zao, natumphira m'khamu,
15. napfuula Dati, Anthuni, bwanji mucita zimenezi? ifenso tiri anthu a mkhalidwe wathu umodzimodzi ndi wanu, akulalikira kwa inu Uthenga Wabwino, wakuti musiye zinthu zacabe izi, nimutembenukire kwa Mulungu wamoyo, amene analenga zakumwamba ndi zapansi, ndi nyanja, ndi zonse ziri momwemo:
16. m'mibadwo, yakale iye adaleka mitundu yonse iyende m'njira mwao.
17. Koma sanadzisiyira iye mwini wopanda umboni, popeza anacita zabwino, nakupatsani inu zocokera kumwamba mvulaodi nyengoza zipatso, ndi kudzaza mitima yanu ndi cakudya ndicikondwero.
18. Pakunena izo, anabvutika pakuletsa makamu kuti asapereke nsembe kwa iwo.
19. Ndipo anafika kumeneko Ayuda kucokera ku Antiokeya ndi Ikoniyo; nakopa makamu, ndipo anamponya Paulo miyala, namguzira kunja kwa mudzi; namuyesa kuti wafa.
20. Koma pamene, anamzinga akuphunzirawo, anauka iye, nalowa m'mudzi; m'mawa mwace anaturuka ndi Barnaba kunka, ku Derbe.

**Mafunso**

1. Kodi munthu wa ku Lustra anali ndi bvuto lotani? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
2. Ndi ciani cimene cinacitika pamene Paulo anati 'Taimirira'? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
3. Kodi anthu a ku Lustra anaganiza ciani za Paulo ndi Barnaba? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
4. Kodi anthuwo anafuna kucita ciani? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
5. Kodi Paulo ndi Barnaba anawayankha bwanji? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
6. Kodi Paulo anatanthauza ciani pa kunena kuti anthu a ku Lustra anayenera kusiya zinthu zacabe? Kodi m'umoyo mwanu mulinso zinthu zacabe?
7. Ndi ciani cimene cinacitika ndi Paulo kulingana ndi ndime ya 19?
8. Kodi Paulo anafadi? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?

**Sewero**

Lembani malembo pa malo ao kukapeza yankho (Macitidwe a Atumwi 14.15).

| | | | | | | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| **1** | **11** | **21** | **12** | **1** | **12** | **9** | **11** | **9** | **18** | **1** |
| | | | | | | | | | | |

| | | |
|---|---|---|
| **11** | **23** | **1** |
| | | |

| | | |
|---|---|---|
| **9** | **14** | **21** |
| | | |

| | | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|---|
| **21** | **20** | **8** | **5** | **14** | **7** | **1** |
| | | | | | | |

| | | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|---|
| **23** | **1** | **2** | **23** | **9** | **14** | **15** |
| | | | | | | |

| | | | | | | | | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| **1** | **2** | **3** | **4** | **5** | **6** | **7** | **8** | **9** | **10** | **11** | **12** | **13** |
| A | B | C | D | E | F | G | H | I | J | K | L | M |

| | | | | | | | | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| **14** | **15** | **16** | **17** | **18** | **19** | **20** | **21** | **22** | **23** | **24** | **25** | **26** |
| N | O | P | Q | R | S | T | U | V | W | X | Y | Z |

## 5. Paulo ku Efeso

**Macitidwe a Atumwi 19.1-20**

1. Ndipo panali, pamene Apolo anali ku Korinto, Paulo anapita pa maiko a pamtunda, nafika ku Efeso, napeza akuphunzira ena;
2. ndipo anati kwa iwo, Kodi munalandira Mzimu Woyera pamene munakhulupira? Ndipo anati, lai, sitinamva konsekuti Mzimu Woyera waperekedwa.
3. Ndipo anati, Nanga mwabatizidwa m'ciani? Ndipo anai, Mu ubatizo wa Yohane.
4. Ndipo anati Paulo, Yohane anabatiza ndi ubatizo wa kutembenuka mtima, nati kwa anthu, kuti amkhulupirire iye amene adzadza pambuyo pace, ndiye Yesu.
5. Pamene anamva ici, anabatizidwa m'dzina la Ambuye Yesu.
6. Ndipo pamene Paulo anaika manja ace pa iwo, Mzimu Woyera anadza pa iwo; ndipo analankhula ndi malilime, nanenera.
7. Onsewo anali ngati amuna khumi ndi awiri.
8. Ndipo iye analowa m'sunagoge, nanena molimba mtima, miyezi itatu, natsutsana ndi kukopa kunena za Ufumu wa Mulungu.
9. Koma pamene ena anaumitsa mtima ndi kusamvera, nanenera zoipa Njirayo pamaso pa anthu, anawacokera, napatutsa akuphunzira, nafotokozera masiku onse m'sukulu ya Turano.
10. Ndipo anacita comweco zaka ziwiri; kotero kuti onse akukhala m'Asiya anamva mau a Ambuye, Ayuda ndi Ahelene.
11. Ndipo Mulungu anacita zamphamvu za pa zokha ndi manja a Paulo;
12. kotero kuti anamuka nazo kwa odwala nsaru zopukutira ndi za panchito, zocokera pathupi pace, ndipo nthenda zinawacokera, ndi mizimu yoipa inaturuka.
13. Koma Ayuda enanso oyendayenda, oturutsa ziwanda, anadziyesa kuchula pa iwo amene anali ndi mizimu yoipa dzina la Ambuye Yesu, kuti, Ndikulumbirirani pa Yesu amene amlalika Paulo.
14. Ndipo panali ana amuna asanu ndi awiri a Skeva, Myuda, mkuru wa ansembe amene anacita ici.
15. Ndipo unayankha mzimu woipa, nuti kwa iwo, Yesu ndimzindikira, ndi Paulo ndimdziwa, koma inu ndinu ayani?
16. Ndipo munthu, mwa iye amene munali mzimu woipa, anawalumphira nawaposa, nawalaka onse awiriwo, kotero kuti anathawa m'nyumba amarisece ndi olasidwa.
17. Zimenezo zidamveka kwa onse, Ayuda ndi Ahelene, amene anakhala ku Efeso; ndipo mantha anagwera onsewo, ndipo dzina la Yesu linakuzika.
18. Ndipo ambiri a iwo akukhulipirawo anadza, nabvomereza, nafotokoza macitidwe ao.
19. Ndipo ambiri a iwo akucita zamatsenga anasonkhanitsa mabuku ao, nawatentha pamaso pa onse; ndipo anawerenga mtengo wace, napeza ndalama zasiliva zikwi makumi asanu.
20. Cotero mau a Ambuye anacuruka mwamphamvu nalakika.


**Mafunso**

1. Kodi Paulo anafika kuti? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
2. Kodi Paulo anafunsa ciani anthu a ku Efeso? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
3. Kodi anthu anamuyankha ciani? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
4. Nanga inu mudziwa ciani za Mulungu Mzimu Woyera?
5. Werenganinso ndime ya 9. Kodi anthu anayankha bwanji atamva mau a Paulo?
6. Nanga inu mumayankha bwanji mutamva Mau a Mulungu?
7. Kulingana ndi ndime ya 13 kunali anthu oturutsa ziwanda amene anachula dzina la Yesu koma sanali anthu a Mulungu. Kodi tingadziwe bwanji zosiyana za anthu a Mulungu ndi anthu ena amene amagwiritsa cabe dzina la Mulungu?
8. Anthu ambiri amene anakhulupirira mwa Yesu anatentha mabuku ao oipa. Kodi m'umoyo mwanu mulinso zinthu zoipa zimene ziyenera kucotsedwa?

**Sewero**

Lembani mau pa malo ao kukapeza yankho

- Efeso
- Skeva
- manja
- Yesu
- Ayuda
- Apolo
- nsaru
- Mzimu
- Korinto
- kulandira
- ufumu
- mtima
- dzina
- ziwiri



## 6. Demetriyo autsa phokoso

### Macitidwe a Atumwi 19.21-40

21. Ndipo zitatha izi, Paulo anatsimikiza mu mzimu wace, atapita pa Makedoniya ndi Akaya, kunka ku Yerusalemu, kuti, Nditamuka komweko ndiyenera kuonanso ku Roma.
22. Pamene anatuma ku Makedoniya awiri a iwo anamtumikira, Timoteo ndi Erasto, iye mwini anakhalabe nthawi m'Asiya.
23. Nthawi yomweyo kunali phokoso lambiri kunena za Njirayo.
24. Pakuti munthu wina dzina lace Demetriyo wosula siliva, amene anapanga tiakacisi tasiliva ta Artemi, anaonetsera amisiri phindu lambiri;
25. amenewo iye anawasonkhanitsa pamodzi ndi amisiri a nchito yomweyo, nati, Amuna inu, mudziwa kuti ndi malonda awa ife tipeza cuma cathu.
26. Ndipo muona ndi kumva, kuti si pa Efeso pokha, koma monga pa Asiya ponse, Paulo uyu akopa ndi kutembenutsa anthu ambiri, ndi kuti, Si milungu iyi imene ipangidwa ndi manja:
27. ndipo tiopa ife kuti nchito yathuyi idzayamba kunyonyosoka; komanso kuti kacisi wa mlungu wamkazi Artemi adzayamba kuyesedwa wacabe; ndiponso kuti iye adzayamba kutsitsidwa ku ukulu wace, iye amene a m'Asiya onse, ndi onse a m'dziko lokhalamo anthu, ampembedza.
28. Ndipo pamene anamva, anadzala ndi mkwiyo, napfuula, nati, Wamkuru ndi Artemi wa ku Efeso,
29. Ndipo m'mudzi monse munacita piringu-piringu, nathamangira onse pamodzi ku bwalo losewera, atagwira Gayo ndi Aristarko, anthu a ku Makedoniya, alendo anzace a Paulo.
30. Ndipo pamene Paulo anafuna kulowa kwa anthu, akuphunzira ace sanamloleza.
31. Ndipo akulu ena a Asiyanso, popeza anali abwenzi ace, anatumiza mau kwa iye, nampempha asadziponye ku bwalo lakusewera.
32. Ndipo ena anapfuula kanthu kena, ena kanthu kena; pakuti msonkhanowo unasokonezeka; ndipo unyinji sunadziwa cifukwa cace ca kusonkhana.
33. Ndipo anaturutsa Alesandro m'khamumo, kumturutsa iye Ayuda. Ndipo Alesandro anatambasula dzanja, nafuna kudzikanira kwa anthu adasonkhanawo.
34. Koma pozindikira kuti ali Myuda, kunali mau amodzi a kwa onse akupfuula monga maora awiri, Wamkuru ndi Artemi wa Aefeso.
35. Ndipo pamene mlembi adatontholetsa khamulo, anati, Amuna a Efeso inu, munthuyu ndani wosadziwa kuti mudzi wa Aefeso ndiwo wosungira kacisi wa Artemi wamkuru, ndi fano lidacokera kwa Zeu?
36. Popeza tsono izi sizikanika, muyenera inu kukhala cete, ndi kusacita kanthu kaliuma.
37. Pakuti mwatenga anthu awa, osakhala olanda za m'kacisi, kapena ocitira mulungu wathu mwano.
38. Ngati tsono Demetriyo ndi amisiri okhala naye, ali ndi mlandu ndi munthu, mabwalo a mirandu alipo, ndi ziwanga ziripo; anenezane.
39. Koma ngati mufuna kanthu ka zinthu zina, kadzakonzeka m'msonkhano wolamulidwa.
40. Pakutinso palipo potiopsya kuti adzatineneza za cipolowe ca lero; popeza palibe cifukwa ca kufotokozera za cipiringu cimene.
41. Ndipo pamene ananena izi, anamasula msonkhano.

**Mafunso**

1. Kodi Demetriyo ankapanga ciani? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
2. M'ndime ya 24 tawerenga kuti Demetriyo anaonetsera amisiri phindu lambiri. Kodi ici citanthauzanji?
3. Kodi Demetriyo anacita ciani atamva kuti anthu ambiri anakhulupirira Yesu m'malo mwa mlungu wamkazi Artemi?
4. Kodi m'moyo mwathu mulinso milungu ina imene imene mumapembedzera cifukwa ca kuganiza kuti idzakupatsani phindu lambiri?
5. Demetriyo anafuna kupeza ndalama pa kugulitsa tiakacisi. Kodi Mulungu atilola kupeza ndalama m'njira yoipa?
6. Kodi anthu anapfuula ciani maora awiri? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
7. Mlembi wa Efeso ananena kuti Paulo sanacite zoipa kwa mlungu wao. Ndi ciani cimene cinacitika pamene ananena tero kulingana ndi ndime ya 41?

**Sewero**

Mutapeza mau onse, lembani yankho mogwiritsa nchito malembo osaphedwa.

| | | | | | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| E | F | E | S | O | R | O | M | A | P |
| M | U | M | L | E | M | B | I | L | H |
| M | A | O | R | A | P | A | U | L | O |
| P | F | U | U | L | A | R | U | D | K |
| A | V | I | L | I | S | T | N | Z | O |
| K | A | C | I | S | I | E | G | I | S |
| U | G | N | U | L | I | M | U | K | O |
| D | E | M | E | T | R | I | Y | O | ! |

- Artemi
- milungu
- Kacisi
- Demetriyo
- phokoso
- pfuula
- maora
- siliva
- Paulo
- Efeso
- mlembi
- Roma

## 7. Paulo mu Trowa

**Macitidwe a Atumwi 20.7-12 ndi 17-30 ndi 35-38**

7Ndipo tsiku loyamba la sabata, posonkhana ife kunyema mkate, Paulo anawafotokozera mau, popeza anati acoke m'mawa
mwace; ndipo ananena cinenere kufikira pakati pa usiku.
8Ndipo munali nyali zambiri m'cipinda ca pamwamba m'mene tinasonkhanamo.
9Ndipo mnyamata dzina lace Utiko anakhala pazenera, wogwidwa nato tulo tatikuru; ndipo pakukhala cifotokozere Paulo,
ndipo pogwidwa nato tulo, anagwa posanja paciwiri, ndipo anamtola wakufa.
10Ndipo potsikirako Paulo, anamgwera namfungatira, nati, Musacite phokoso, pakuti moyo wace ulipo.
11Ndipo m'mene adakwera, nanyema mkate, nadya, nakamba nao nthawi, kufikira kuca, anacokapo,
12Ndipo anadza naye mnyamata ali wamoyo, natonthozedwa kwakukuru.


**Mafunso**

1. Kodi anthu anasonkhana pa tsiku liti kulingana ndi ndime ya 7?
2. Kodi anthuwo anasonkhana kuti? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
3. Kodi ndani amene anakhala pa dzenera?
4. Ndi ciani cimene cinacitika ndi mnyamatayo? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
5. Kodi Paulo anacita ciani atamva kuti Utiko anagwa? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
6. Kodi anthu anamva bwanji pamene anaona mphamvu ya Mulungu? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?

**Sewero**

Lembani mau pa malo ao kukapeza yankho.

| | | |
|---|---|---|
| Aefeso | Utiko | nyumba |
| wakufa | Yesu | mtima |
| Mzimu | nyali | mtengo |
| mpingo | anthu | |



## 8. Amtumiza Paulo ku Roma

**Macitidwe 27.1-13**

1 Ndipo pamene padatsimikizika kuti tipite m'ngalawa kunka ku Italiya, anapereka Paulo ndi andende ena kwa kenturiyo dzina lace Yuliyo, wa gulu la Augusto.
2 Ndipo m'mene tidalowam'ngalawa ya ku Adramutiyo ikati ipite kunka ku malo a ku mbali ya Asiya, dnakankha, ndipo Aristarko Mmakedoniya wa ku Tesalonika, anali nafe.
3 Ndipo m'mawa mwace tinangokoceza ku Sidoni; ndipo Yuliyo anacitira Paulo mwacikondi, namlola apite kwa abwenzi ace amcereze.
4 Ndipo pokankhanso pamenepo, tinapita kutseri kwa Kupro, popeza mphepo inaomba mokomana nafe.
5 Ndipo pamene tidapyola nyanja ya kunsi kwace kwa Kilikiya ndi Pamfiliya, tinafika ku Mura wa Lukiya.
6 Ndipo kenturiyo anapezako ngalawa ya ku Alesandriya, irikupita ku Italiya, ndipo anatilongamo.
7 Ndipo m'mene tidapita pang'ono pang'ono masiku ambiri, ndi kufika mobvutika pandunji pa Knido, ndipo popeza siinatilolanso mphepo, tinai pita m'tseri mwa Krete, pandunji pa Salimone;
8 ndipo popaza-pazapo mobvutika, tinafika ku malo ena dzina lace Pokoceza Pokoma; pafupi pamenepo panali mudzi wa Laseya.
9 Ndipo itapita nthawi yambiri, ndipo unayambokhala woopsya ulendowo, popezanso nyengo ya kusala cakudya idapita kale, Paulo anawacenjeza,
10 nanena nao, Amuna inu, ndiona ine kuti ulendo udzatitengera kuonongeka ndi kutayika kwambiri, si kwa akatundu okha kapena ngalawa yokha, komatunso kwa moyo wathu.
11 Koma kenturiyo anakhulupirira watsigiro ndi mwini ngalawa makamaka, wosasamala mau a Paulo.
12 Ndipo popezadooko silinakoma kugonapo nyengo yacisanu, unyinji unacita uphungu ndi kuti amasule nacokepo, ngati kapena nkutheka afikire ku Foinika, ndi kugonako, ndilo dooko la ku Krete, loloza kumpoto ndi kumwela.
13 Ndipo poomba pang'ono mwela, poyesa kuti anaona cofunirako, anakoka nangula, napita m'mbali mwa Krete.

**Mafunso**

1. Kodi Paulo anapita bwanji ku Roma? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
2. Ndi cifukwa ciani ulendo unatenga nthawi yaitali? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
3. Kodi Paulo anapereka upangiri wotani kwa kenturiyo? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
4. Kodi kenturiyo anamvera Paulo? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
5. M’Baibulo Mulungu atipangira kuti tidzipereka kwa Iye. Kodi mumvera upangiri uwu?

**Sewero**

Lembani mau pa malo ao kukapeza yankho.

| | | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|---|
| | P | | … | | | |
| | G | | … | | | |
| | | y | … | | | |
| N | | | … | | | |
| | | | D | | | |
| | | R | … | | | |

| | | |
|---|---|---|
| nyanja | ndi | nyengo |
| Roma | ngalawa | Paulo |

## 9. Tsoka pa nyanja

**Macitidwe a Atumwi 27.14-44**
14 Koma patapita pang'ono idaombetsa kucokerako mphepo ya namondwe, yonenedwa Eurokulo;
15 ndipo pogwidwa nayo ngalawa, yosakhoza kupitanso mokomana nayo mphepo, tidangoleka, ndipo tinangotengedwa.
16 Ndipo popita kutseri kwa cisumbu cacing'ono dzina lace Kauda, tinakhoza kumangitsa bwato koma mobvutika;
17 ndipo m'mene adaukweza, anacita nazo zothandizira, nakulunga ngalawa; ndipo pakuopa kuti angatayike pa Surti, anatsitsa matanga, natengedwa motero.
18 Ndipo pobvutika kwakukuru ndi namondweyo, m'mawa mwace anayamba kutaya akatundu;
19 ndipo tsiku lacitatu anataya ndi manja ao a iwo eni zipangizo za ngalawa.
20 Ndipo m'mene dzuwa kapena nyenyezi sizinatiwalira masiku ambiri, ndipo namondwe wosati wamng'ono anatigwera, ciyembekezo conse cakuti tipulumuke cidaticokera pomwepo.
21 Ndipo pamene atakhala nthawi yaikuru osadya kanthu, Paulo anaimirira pakati pao, nati, Amuna inu, mukadamvera ine, osacoka ku Krete, osadzitengera kuonongeka ndi kutayika kumene.
22 Koma tsopano ndikucenjezani mulimbike mtima; pakuti sadzatayika wamoyo mmodzi mwa inu, koma ngalawa ndiyo.
23 Pakuti anaimirira kwa ine usiku walero mngelo wa Mulungu amene ndiri wace, amenenso ndimtumikira,
24 nanena, Usaope Paulo; ukaimirira pamaso pa Kaisara; ndipo, taona, Mulungu anakupatsa onse amene akuyenda nawe pamodzi.
25 Cifukwa cace, limbikani mtima, amuna inu; pakuti ndikhulupirira Mulungu, kuti kudzatero monga momwe ananena ndi ine.
26 Koma tiyenera kutayika pa cisumbu cakuti.
27 Koma pofika usiku wakhumi ndi cinai, potengedwa ife kwina ndi kwina m'nyanja ya Adriya, pakati pa usiku amarinyero anazindikira kuti analikuyandikira kumtunda;
28 ndipo anayesa madzi, napeza mikwamba makumi awiri; ndipo katapita kanthawi, anayesanso, napeza mikwamba khumi ndi isanu.
29 Ndipo pakuopa tingatayike pamiyala, anaponya anangula anai kumakaliro, nakhumba kuti kuce.
30 Ndipo m'mene amarinyero anafunakuthawa m'ngalawa, natsitsira bwato m'nyanja, monga ngati anati aponye anangula kulikuru,
31 Paulo anati kwa kenturiyo ndi kwa asilikari, Ngati awa sakhala m'ngalawa inu simukhoza kupulumuka.
32 Pamenepo asilikari anadula zingwe za bwato, naligwetsa.
33 Ndipo popeza kulinkuca, Paulo anawacenjeza onse adye kanthu, nati, Lero ndilo tsiku lakhumi ndi cinai limene munalindira, ndi kusala cakudya, osalawa kanthu.
34 Momwemo ndikucenjezani mutenge kanthu kakudya; pakuti kumeneku ndi kwa cipulumutsocanu; pakuti silidzatayika tsitsi la pa mutu wa mmodzi wa inu.
35 Ndipo atanena izi, ndi kutenga mkate, anayamika Mulungu pamaso pa onse; ndipo m'mene adaunyema anayamba kudya.
36 Ndipo anakhala olimbika mtima onse, natenga cakudya iwo omwe.
37 Ndipo life tonse tiri m'ngalawa ndife anthu mazana awiri mphambu makumi asanu ndi awiri kudza asanu ndi mmodzi.
38 Ndipo m'mene anakhuta, anapepuza ngalawa, nataya tirigu m'nyarija.
39 Ndipo kutaca sanazindikira dzikolo; koma anaona pali bondo la mcenga; kumeneko anafuna, ngati nkutheka, kuyendetsako ngalawa.
40 Ndipo m'mene anataya anangula anawasiya m'nyanja, namasulanso zingwe zomanga tsigiro; ndipo pokweza thanga la kulikuru, analunjikitsa kumcenga.
41 Koma pofika pamalo pokomana mafunde awiri, anatsamitsapo ngalawa; ndipo kulikuru kunatsama, ndi kukhala kosasunthika, koma kumakaliro kunasweka ndi mphamvu ya mafunde.
42 Ndipo uphungu wa asilikari udati awapheandende, angasambire, ndi kuthawa.
43 Koma kenturiyo, pofuna kupulumutsa Paulo, anawaletsa angacite ca uphungu wao; nalamula kuti iwo akukhoza kusambira ayambe kudziporiya m'nyanja, nafike pamtunda,
44 ndipo otsalawo, ena pamatabwa, ndi ena pa zina za m'ngalawa. Ndipo kudatero kuti lonse adapulumukira pamtunda.

**Mafunso**

1. Chulani dzina la mphepo ya namondwe. Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
2. Anthu amene anali m'ngalawa anakomana ndi mabvuto. Kodi anacita ciani kudzipulumutsa kulingana ndi ndime za 17, 18 ndi 19?
3. Kodi mumayesa kudzipulumutsa m'malo mwa kudalira pa Mulungu yekha?
4. Kodi Paulo anadziwa bwanji kuti onse adzapulumutsidwa? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
5. Masiku ano Mulungu amalankhula mwa Baibulo. Kodi mumawerenga kapena kumvera Baibulo?
6. Ndi ciani cimene cinacitika usiku wakhumi ndi cinai? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
7. Ndi cifukwa ciani Paulo anadya mkate? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
8. Kulingana ndi ndime ya 43 zonse zimene Mulungu anafotokozera Paulo zinacitika. Anthu onse anapulumutsidwa. Ifenso tiyenera kupulumutsidwa. Kodi tiyenera kupulumutsidwa ku ciani?

## 10. Paulo pa Melita

**Macitidwe a Atuwmi 28.1-10**

1. Ndipo titapulumuka, pamenepo tinadziwa kuti cisumbuco cinachedwa Melita.
2. Ndipo akunja anaticitira zokoma zosacitika pena ponsepo; pakuti anasonkha moto, natilandira ife tonse, cifukwa ca mvula inalinkugwa, ndi cifukwa ca cisanu.
3. Koma pamene Paulo adaola cisakata ca nkhuni, naciika pamoto, inaturukamo njoka, cifukwa ca kutenthaku, niluma dzanja lace.
4. Koma pamene akunjawo anaona ciromboco ciri lende pa dzanja lace, ananena wina ndi mnzace, Zoona munthuyu ndiye wambanda, angakhale anapulumuka m'nyanja, cilungamo sicimlola akhale ndi moyo.
5. Koma anakutumulira ciromboco kumoto, osamva kupweteka.
6. Koma anayesa kuti adzatupa, kapena mwini wace kugwa kufa pomwepo; koma m'mene adalindira nthawitu, naona kuti sikunampweteka, anapindula, nati, Ndiye Mulungu.
7. Koma pafupi pamenepo panali minda, mwini wace ndiye mkulu cisumbuco, dzina lace Popliyo; amene anatilandira ife, naticereza okoma masiku atatu.
8. Ndipo kunatero kuti atate wace wa Popliyo anagona wodwala nthenda ya malungo ndi kamwazi. Kwa iyeyu Paulo analowa, napemphera, naika manja pa iye, namciritsa.
9. Ndipo patacitika ici, enanso a m'cisumbu, okhala nazo nthenda, anadza, naciritsidwa;
10. amenenso anaticitira ulemu wambiri; ndipo pocoka ife anatiikira zotisowa.

**Mafunso**

1. Kodi Paulo ndi anthu opulumutsidwa m'mphepo ya namondwe anali pa cisumbu citi? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
2. Kodi akunja anawacitira ciani? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
3. Nanga ife timacitira ciani anthu amene ali m'mabvuto?
4. Fotokozani zimene zinacitika atalumidwa Paulo ndi njoka. Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
5. M'Luka 10.19 ndi 20 tiwerenga, 'Taonani, ndakupatsani ulamuliro wakuponsa pa njoka ndi zinkhanira, ndi pa mphamvu iri yonse ya mdaniyo; ndipo kulibe kanthu kadzakuipsani konse. Koma musakondwera nako kuti mizimu idakugonjerani, koma kondwerani kuti maina anu alembedwa m'Mwamba. Kulingana ndi ndime izi ndi ciani cimene cofunikira copambana: kucita zodabwitsa kapena kudziwa Yesu kuti dzina lanu lalembedwa m'Mwamba?
6. Fotokozani zimene zinacitika ndi atate wace wa Popliyo. Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?

**Sewero**

Pezani mau onse.

| | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|
| N | M | M | O | T | O |
| J | K | U | A | L | L |
| O | O | H | L | U | U |
| K | M | N | U | G | A |
| A | A | U | V | N | P |
| E | N | E | M | A | I |

moto
nkhuni
njoka
koma
amene
mvula
Paulo

## 11. Paulo afika ku Roma

**Macitidwe a Atumwi 28.11-31**
11 Ndipo itapita miyezi itatu tinayenda m'ngalawa ya ku Alesandriya, idagonera nyengo ya cisanu kucisumbuko, cizindikilo cace, Ana-a-mapasa.
12 Ndipo pamene tinakoceza ku Surakusa, tinatsotsako masiku atatu.
13 Ndipo pocokapo tinapaza ntifika ku Regio; ndipo litapita tsiku limodzi unayamba mwela, ndipo m'mawa mwace tinafika ku Potiyolo:
14 pamenepo tinakomana ndi abale, amene anatiumirira tikhale nao masiku asanu ndi awiri; ndipo potero tinafika ku Roma.
15 Kucokera kumeneko abalewo, pakumva za ife, anadza kukomana nafe ku Bwalo la Apiyo, ndi ku Nyumba za Alendo Zitatu; ndipo pamene Paulo anawaona, anayamika Mulungu, nalimbika mtima.
16 Ndipo pamene tinalowa m'Roma, analola Paulo akhale pa yekha ndi msilikari womdikira iye.
17 Ndipo kunali, atapita masiku atatu, anaitana akulu a Ayuda asonkhane; ndipo atasonkhana, ananena nao, Ine, amuna, abale, ndingakhale sindinacita kanthu kakuipsa anthu, kapena miyambo ya makolo, anandipereka wam'nsinga kucokera ku Yerusalemu ku manja a Aroma;
18 ndiwo, atandifunsafunsa ine anafuna kundimasula, popeza panalibe cifukwa ca kundiphera.
19 Koma pakukanapo Ayuda, ndinafulumidwa mtima kuturukira kwa Kaisara; si kunena kuti ndinali nako kanthu kakunenera mtundu wanga.
20 Cifukwa ca ici tsono ndinakupemphani inu mundione ndi kulankhula nane; pakuti cifukwa ca ciyembekezo ca Israyeli ndamangidwa ndi unyolo uwu.
21 Ndipo anati kwa iye, Ife sitinalandira akalata onena za inu ocokera ku Yudeya, kapena sanadza kuno wina wa abale ndi kutiuza kapena kulankhula kanthu koipa ka inu.
22 Koma tifuna kumva mutiuze muganiza ciani; pakuti za mpatuko uwu, tidziwa kuti aunenera ponse ponse.
23 Ndipo pamene adampangira tsiku, anadza ku nyumba yace anthu ambiri; amenewo anawafotokozera, ndikucitira umboni Ufumu wa Mulungu, ndi kuwakopa za Yesu, zocokera m'cilamulo ca Mose ndi mwa aneneri, kuyambira mamawa kufikira madzulo.
24 Ndipo ena anamvera zonenedwazo, koma ena sanamvera.
25 Koma popeza sanabvomerezana, anacoka atanena Paulo mau amodzi, kuti, Mzimu Woyera analankhula kokoma mwa Yesaya Mneneri kwa makolo anu,
26 ndi kuti, Pita kwa anthu awa, nuti, Ndi kumva mudzamva, ndipo simudzazindikira konse; Ndipo pakupenya mudzapenya, koma osaona konse;
27 Pakuti mtima wa anthu awa watupatu, Ndipo m'makutu mwao mmolemakumva, Ndipo masoao anawatseka; Kuti angaone ndi maso, Nangamve ndi makutu, Nangazindikire ndi mtima, Nangatembenuke, Ndipo Ine ndingawaciritse.
28 Potero, dziwani inu, kuti cipulumutso ici ca Mulungu citumidwa kwa amitundu; iwonsoadzamva.
30 Ndipo anakhala zaka ziwiri zamphumphu m'nyumba yace yobwereka, nalandira onse akufika kwa iye,
31 ndi kulalikira Ufumu wa Mulungu, ndi kuphunzitsa za Ambuye Yesu Kristu ndi kulimbika konse, wosamletsa munthu.

**Mafunso**
1. Paulo atafika ku Roma, ndi ciani cimene cinacitika? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
2. Werenganinso ndime ya 20. Kodi ciyembekezo ca Israyeli ndi Yani?
3. Nanga ciyembekezo canu ndi ciani?
4. Paulo anamangidwa koma analalikirabe cipulumutso mwa Yesu. Nanga inunso mumafalitsa Uthenga wabwino pamene muli m'mabvuto?
5. Werenganinso ndime ya 24. Nanga inu, mukhulupirira moonadi kapena simumvera Mau a Mulungu?